



Ndikwaniritsa zomwe ndidalonjeza - Chakwera

WOLEMBA:
MANASE NYIRENDA

BOMA lakangalika ndi ntchito zachitukuko zosiyanasiyana mmadera ambiri mdziko muno. Posachedwapa, Mtsogoleri wa dziko lino a Lazarus Chakwera anatsimikizira Amalawi kuti boma lawo lipitirira kukwaniritsa zomwe lidalonjeza ndicholinga chotukula dziko lino ndikuonetsetsa kuti anthu akukhala moyo wabwino.

Poyankhula masiku apitawa atatsegulira sukulu zosula aphunzitsi za Rumphu, Chikwawa ndi Mchinji, zomwe zikweze chiwerengero cha ophunzira mmasukuluwa kuchoka pa 4,000 kufika pa 6,200, iwo anati chitukuko chamaphunziro ndichofunika kwambiri posintha anthu kuti akhale ozidalira

ZA BOMA



Wojambula: Lisa Kadango

Dr Lazarus Chakwera kuyendera chitukuko chamaofesi pa Konsolo ya Mmbelwa

mmagawo osiyanasiyana.

“Pofuna kutukula maphunziro tiyenera kukhala ndi aphunzitsi ndi sukulu zokwanira ndicholinga choti maphunziro afikire pali ponse. Pokwaniritsa izi Boma likuyetsetsa kutsegula sukulu zochulukira zosula aphunzitsi mdziko muno ndipo umboni wake ndikutsegulira kwasukulu lero.

“Sukulu zamangidwa mwamakono kwambiri chifukwa zili ndi malo ophunziriramo makina akompyuta komanso ntchito zaluso lamanja monga zosemasema, zootchelera mwa zina,” adatero a Chakwera.

Mtsogoleriyu anatinso ngati njira yolimbikitsa chitukuko mmadera onse mdziko lino, Boma lakweza ndalama zachitukuko zammadera a aphungu kuchoka pa 40 miliyoni kufika pa 200 miliyoni kwacha kuti zikwanitse kubweretsa chitukuko chosiyanasiyana mmaderawo monga sukulu, zipatala, milatho ndi zina.

Nduna ya zamaphunziro a Madalitso Kambauwa Wilima, anati sukulu zosula aphunzitsi zikwanitsa kupititsa patsogolo luso losiyanasiyana ndipo

» TSAMBA 2

ZAUMOYO

WOLEMBA:
GEORGE MPONDA,
IREEN MSETIKA NDI
RENNIE TEMBO

Pamene nthenda yamaso ikufala kwambiri mdziko lino, anthu ena ayamba kugwiritsa ntchito njira zosavomerezeka zomwe a Unduna wa zaumoyo ati zikhoza kuika miyoyo yawo pa chiopsezo.

Mkulu wazaumoyo m'boma

Nthenda yamaso yavuta, tisamale!

la Karonga, a David Sibale anati ena akugwiritsa ntchito mankhwala ophera tizilombo toyambitsa matenda mmanja komanso mikodzo zomwe zili zosayenera kuthiridwa mmaso. Iwo alangiza anthu omwe akuchita mchitidwewu kuti asiye chifukwa akhoza kuononga maso awo, pomwe

anaonjezera kuti sikoyenera kuti munthu azithira mikodzo ndi zinthu zina mmaso. “Tawona kuti anthu akugwiritsa ntchito zinthu monga mikodzo ndi mankhwala osambira mmanja ngati njira imodzi yodzitetezera komanso kuzichiritsa ku matenda amasowa.

“Izi ndizowopsa chifukwa mikodzo ili ndi tizilombo tambiri tomwe tikalowa mmaso tikhoza kupangitsa kuti munthu achite khungu komanso kutenga chizonono chammaso,” adatero a Sibale.

Pofuna kuonetsetsa kuti uthengawu ukufikila anthu ambiri, Mkulu wa zaumoyo

m'boma la Likoma, a Gabriel Chipeta ati awonetsetsa kuti anthu afikiridwe ndi tsatanetsatane woyenera kutsata pothana ndi kupewa nthendayi.

“Tipitiliza kudziwitsa anthu za momwe angadzitetezere kunthendayi kudzera mu zokambirana za zaumoyo m'zipatala komanso kudzera pawalesi.

» TSAMBA 3



Mayi wa fuko alimbikitsa ophunzira

» TSAMBA 3



Alimi alimbikitsidwa kusamala fodya

» TSAMBA 6



Achinyamata 700 aphunzira ntchito zamanca

» TSAMBA 10

Ndemanga

Boma likukwaniritsa malonjezo

KUYENDA mmaboma ambiri mdziko lino, tikuona ntchito zosiyanasiyana zachitukuko zomwe zikuchitika mokwaniritsa zomwe Boma linawalonjeza Amalawi pamene limatenga ulamuliro wadziko lino. Mtsogoleri wadziko lino wakhala akutsimikizira anthu kuti awonetsetsa kuti chitukuko chifikire madera onse mdziko lino.

Umboni pankhaniyi ndi ulendo omwe mtsogoleriyu anali nawo posachedwapa oyendera chitukuko chosiyanasiyana mchigawo chakumpoto. A Chakwera awonetsa kuti sakusankha madera pofuna kufikira anthu ndi chitukuko. Iwo akufunitsitsa kuti dziko la Malawi litukuke ngati maiko ena onse omwe ali otsogola pachitukuko.

Dziko la Malawi likhoza kutukuka ndikukwanilitsa zomwe mtsogoleri wake akufuna ngati tingamuthandize kukwaniritsa malotowa. Izi zikhoza kutheka ngati Amalawi tingatengepo mbali polimbikitsa ndikuthandiza mtsogoleri wathu kubweretsa chitukuko mmadera mwathu.

Pali ena omwe ngakhale angaone zomwe zikuchitika mmadera awo, amasankha kusavomera kuti kudera kwawo kukuchitika chitukuko. Mkhaliidwe uwu ndi owwezeretsa mmbuyo chitukuko chadziko chifukwa anthu otere sangatenge nawo mbali pachitukuko pazifukwa zawo zandale.

Zimene Amalawi awona kuchigawo chakumpoto zikupereka chiyembekezo kuti dziko lathu likhoza kutukuka mmagawo osiyanasiyana ngati mtsogoleriyu alimbikitsidwa kukwanilitsa masomphenya ake pachitukuko cha dziko lino.

Nduna iyamikira ulimi wa nsomba



Ulimi wansomba ndi opindulitsa kwambiri

WOLEMBA:
LEAH MALIMBASA

MU ulimi muli phindu. Atsogoleri amalimbikitsa ulimi osiyanasiyana pozindikira kuti ngati mbali ina yaulimi yavuta, mlimi azitha kupezabe phindu kuchokera ku ulimi wina. Kupatula ulimi wambewu zakumunda alimi amalimbikitsidwa kupanganso

ulimi wa ziweto komanso nsomba. Nduna yooka za chilengedwe ndikusintha kwa nyengo a Micheal Usi ati ulimi wa nsomba uli ndikuthekera kotukula chuma cha dziko lino ndikubweretsa ndalama zakunja zochuluka ku dziko lino la Malawi. Iwo ananena izi pamene amayendera nyumba ya ulimi wa nsomba ya Kasinthula mboma la Chikwawa. Iwo adati “Ngati tikufuna kutukula dziko lino, tikuyenera kugulitsa katundu wathu kumaiko akunja. Nsomba ndi

imodzi mwa zinthu zomwe tingamagulitse kunja ndipo pakali pano ulimi wa nsomba wayamba kale kuchita bwino,” “Mmbuyomu timachita kuyitanitsa chakudya chopatsa nsomba koma pakali pano tayamba kupanga tokha zakudyazi kutanthauza kuti ulimi wa nsomba ukupita patsogolo. Tikufuna kutukula chuma cha dziko lino kudzera mu ulimi wa nsomba ndichifukwa chake lero lino tikukambilana zotsegula malo owetela nsomba ku Kasinthula kuno,” adatero a Usi. Iwo adati ndikofunika kuyenda limodzi powonetsetsa kuti ulimiwu upite patsogolo ndipo sikoyenera kuti papezeke wina osokoneza ntchitoyi. “Kukhala kukubwela anthu ofuna kuyika chuma chawo ku ulimi umenewu, sikoyenera kuti wina alepheletse ntchito yopititsa patsogolo ulimiwu pochedwa kusayinila zikalata kapena zilolezo. Tikufunika tionetsetse kuti pakutha pazaka ziwiri, dziko lino likhale litatukuka ku nkhani za ulimi wa nsomba.

“Tikuyesetsanso kuphunzira zina ndi zina ku maiko omwe adapita patsogolo ku nkhani za ulimi wa nsomba ndipo tikufufuza njira zokopera alendo ndi amalonda omwe akufuna kuyika chuma chawo mu ulimi umenewu kuti atithandize. Malo komanso madzi ochitira ulimiwu alipo koma likusowa ndi thandizo la ndalama,” anaonjezera a Usi. A Usi adaonjezeranso kuti boma likulingalila zokhazikitsa malo ena asanu ndi atatu ochitirapo ulimi wa nsomba. Wachiwiri kwa mkulu oyang'anira ulimi wa nsomba mdziko muno, a Brino Chiriwa adati malo a Kasinthula omwe akhazikitsidwa ngati malo amodzi ochitirapo ulimi wa nsomba ndi malo akulu kwambiri okwana ma hekitala mazana atatu ndipo atati agwiritsidwe ntchito bwino akhoza kubweretsa phindu la nsomba lochuluka. Iwo adati malo a Kasinthula ali ndikuthekera kotukula ulimi wa nsomba mdziko muno chifukwa malowa akhoza kumatulutsa matani 3000 a nsomba. “Boma layika chidwi chake chambiri kuonetsetsa kuti malo a Kasinthula akhale malo apamwamba monga kumanga nyumba zoweteramo nsomba, chipinda chochitiramo kafukufuku osiyanasiyana komanso malo ophunzitsira ukadaulo oweta nsomba pofuna kulimbikitsa ndikuphunzitsa alimi a nsomba,” anatero a Chirwa.

Wojambula: lea Malimbasa

Nthenda yamaso yavuta, tisamale!

«YACHOKERA PA TSAMBA

“Tikukonzekeranso kukhala ndi misonkhano yokambirana ndi atsogoleri am'madera ndipo talemba kalata msukulu kuwadziwitsa zamliwiriwu ndi njira zake zopewera nthendayi, yomwe ena akuyitchula kuti nthenda ya Ng'ombo imene yafika paliponse mdziko muno zomwe zikudandaulitsa ogwira ntchito zaumoyo. Mmodzi wa ogwira ntchito pachipatala cha Bwaila mumzinda wa Lilongwe,

a Isaac Kumwenda adandaula ndi momwe nthendayi ikufalila. Iwoati chifukwa chakufalikira kwa nthendayi, chipatala cha bwaila chikulandira anthu ofuna thandizo la mankhwala ambiri ngakhale chipatalachi chilibe mankhwala okwanira. “Mliri ulipo ndipo ndi mmene ukufalira, tili ndi nkhwana kwambiri chifukwa tilibe mankhwala okwanira, “Tikupempha akufuna



A Esther Mapomba anayeserapo kuthira mkodzo mmaso ngati mankhwala

kwabwino kuti atithandize kupeza mankhwala ndizipangizo zina zogwirira ntchito polimbana ndi nthendayi,” adatero a Kumwenda, Iwo ananenso kuti pakufunika misonkhano yambiri yodziwitsa anthu ndikuwalimbikitsa za kapewedwe ka nthendayi. Nthenda ya ng'ombo ndi nthenda yomwe ikumafalikira mosavuta kuchokera kwa munthu kupita kwa munthu wina ndipo zizindikiro zake ndi monga; kufira kwa maso, kupweteka, kusawona bwino, kumwa kuwawa mutu, kutuluka misonzi ndi kupweteka kwa thupi mwachilendo.

Wojambula: Nkhokwe yathu

ZA MAPHUNZIRO

WOLEMBA:
YAMIKANI SABOLA

MAPHUNZIRO ndimaziko a chitukuko cha dziko ina liri lonse. Koma mavuto azachuma amapangitsa ophunzira ambiri kusiya sukulu zomwe zimakhudza tsogolo lawo. Pozindikira kufunika kwamaphunziro, boma ndi mabungwe akuyesetsa kupereka thandizo kwa ophunzira ovutika kuti asatsalire mmbuyo pamaphunziro. Posachedwapa, Mayi wa fuko lino, a Monica Chakwera, anatenga mbali kulimbikitsa ophunzira kuti azilimbikira pa maphunziro awo kuti azakwaniritse masomphenya awo ngakhale akukumana ndi mavuto osiyanasiyana.

Mayi Chakwera, adanena izi pasukulu ya Mzuzu sekondale pamene amakachezera ophunzira omwe akupindula ndi bungwe lawo lotchedwa Shaping our Future Foundation (SOFF) limene likulipirira fizi ophunzirawa. Iwo adafotokoza ophunzirawa mbiri ya moyo wawo komanso za mmene sakadakwanitsira kupitiriza maphunziro awo chifukwa cha mavuto ngati omwewa. “Makolo anga sankakwanitsa kundiripirira maphunziro kufikira kalasi ya folomu 4. Iwowa adakwanitsa kulipira kalasi ya folomu 1 ndi folomu 2 yokha popeza adalowa



Mai Chakwera kulimbikitsa atsikana a sukulu ya sekondale ya Mzuzu

mungongole, choncho ndidatsala pang'ono kusiya sukulu. “Masiku amenewo, ndi satifiketi ya JCE, timathabe kugwira nayo ntchito ya unamwino komanso uphunzitsi koma sindimafuna kusiira maphunziro anga pa folomu 2 chifukwa ndidali ndi khumbo lofuna kupitiriza maphunziro anga. Mwachisomo cha Mulungu, ndidathandizidwa ndi bungwe la Save the Children limene lidandilipirira malasi a folomu 3 ndi 4,” adatero pofotokozza. Mayi Chakwera adatinso

mbiri yawoyi ndi imene idawalimbikitsa kuyambitsa ntchito yolipirira ophunzira pamaphunziro awo kudzera ku bungwe lawo la SOFF ndikuonetsetsa kuti anyamata ndi asungwana omwe alibe kuthekera, akupeza mwayi omaliza maphunziro awo a sekondale. Wachiwiri kwa Nduna yazamaphunziro, a Nancy Mdooko, adayamikira mayi wa fukoyu polipirira ndalama ophunzirawa pozindikira kuti vuto la zachuma ndi



Wojambula: Lisa Malongo

vuto lina lalikulu limene likulepheretsa ophunzira ambiri kupitiriza maphunziro awo. AMdookoadatibomakudzera mu unduna wa zamaphunziro likuonjezera mwayi olipirira ophunzira maphunziro msukulu za sekondale. “Chiwerengero cha ophunzira amene akupindula ndi ndondomeko imeneyi chaonjezedwa kuchoka pa ophunzira 30,138 kufika 42,043 zimene zikuonetsera kuti chiwerengerochi chakwera ndipo chaposa chiwerengero

chimene chidasindikizidwa mu ndondomeko ya zachuma chamaphunziro (NESP) ya chaka cha 2025 imene ikufuna kufikira ophunzira 40,000,” adatero mayi Mdooko. Wachiwiri kwa ndunayi, anatinso ngakhale chiwerengerochi chakwera mzaka za mmbuyozi, pali ophunzira 19,105 amene akuvutikabe msukulu za sekondale zosiyanasiyana amene akufunikanso mwayi wa ndondomeko imeneyi.

Ndikwaniritsa zomwe ndidalonjeza - Chakwera

«YACHOKERA PA TSAMBA

posachedwapa sukuluzi zizipereka maphunziro a Dipuloma komanso Digiri zamaphunziro a pulayimale. Iwo anati kupatula izi, boma layambanso kumanga nyumba za aphunzitsi 10,000 zomwe zimangidwe mdziko muno pofuna kupereka chisamaliro chabwino kwa aphunzitsi.

Mfumu yaikulu Chikulamayembe ya m'boma la Rumphu, inati sukulu zosula aphunzitsizi zithandiza kukweza maphunziro chomwe ndichitukuko chofunika kwambiri mdziko muno.

Ntchito yomanga sukulu zosula aphunzitsiyi ndiyandalama zokwana \$34 Miliyoni yaku Amerika yomwe ikuperekedwa ndi Boma la Malawi komanso bungwe la Opec.



Chitukuko cha bwalo lazamasewero la Mmbelwa ku Mzimba

Wojambula: Lisa Malongo

Khonsolo ya Lilongwe ilimbikitsa katemera wa chikuku

WOLEMBA
MONICA TAMBALA

CHIKUKU ndi imodzi mwa nthenda zomwe zimapereka chiopsezo ku miyoyo ya ana muno mMalawi. Pamene matenda ena monga Kolera akuvuta ndikupangitsa anthu kusamala motheratu, matenda ena omwe amakhala ngati akuwalika amakhala alipobe ndipo anthu amayenera azikhala akudziwa bwino zakapewedwe kamatendawa. Pachifukwa chicho, posachedwapa khonsolo ya boma la Lilongwe yakhala ikulimbikitsa makolo kuti alandiritse ana awo katemera wa chikuku chomwe chakhudza madera ena mu mzinda wa Lilongwe ndikutenganso miyoyo ya ana awiri. Malinga ndi mneneri wa zaumoyo mukhonsoloyi, a Richard Mvula, anati ana oposa 157 ndi omwe anapezeka



Wazaumoyo kupereka katemera kwa ana.

ndi chikuku ndipo ana 34, 000 adaptatsidwa katemera, mchaka 2023 kufikira 2024. A Mvula anadzudzula khalidwe la anthu ena omwe amafalitsa nkhani zabodza zokhudza katemera zomwe zimapereka mantha kwa anthu ndikuwalepheretsa

kulandira katemera wofunikira. “Pali anthu ena amakonda kufalitsa uthenga wabodza komanso wopanda umboni. Potengera momwe zinalili ndi Covid-19 mchaka cha 2019 mpaka 2020, ena akuona ngati tikumapereka katemera wa Covid-19 kwa ana zomwe ndi zabodza.

Katemera wa Covid sitimapereka kwa ana ang’onoang’ono. Katemera wachikuku ndi wa ana ndipo timapereka kwa ana oyambira miyezi mphambu zisanu ndi zinayi (9) kufika zaka khumi ndi mphambu zisanu (15),” anatero a Mvula. Iwo anati aliyense atakhala kuti akulandira katemera moyenera, miliri yambiri itha kumapewedwa pakati pa anthu. A Mvula anayamikira mabungwe osiyanasiyana monga bungwe la Red Cross lomwe lakhala likufikira mabanja ambiri mdziko muno kuwalimbikitsa ndikuwadziwitsa za nthenda zosiyanasiyana kuphatikizapo chikuku. Mkulu owona za umoyo ndi thandizo la anthu ku bungwe la Red Cross, a Dan Kapombosola Banda adatsindika kuti bungwe lawo likhala likupitiliza kupereka thandizo ku boma la Malawi kuti lifikire mabanja ambiri ndi kutetedza miyoyo ya ana mdziko muno. “Red Cross ndi limodzi mwa

mabungwe omwe angathandize kuonetsetsa kuti tagonjetsa chikuku chomwe chabwera pakati pathu. Ife a Red Cross timagwira ntchito kwambiri ndi anthu ozipereka, ndipo tikudziwa kuti mavuto amenewa akuchokera kumudzi ndipo kuti vutoli lithe tikuyenera kuyamba kuthana nalo kumudzi komweko, Tikuonesetsa kuti mauthenga akupita moyenera kwa anthu, ndipo ogwira ntchito zaumoyo alandira maphunziro oyenera kuti athandize kumema anthu kuti ana awo akalandire katemera wa chikuku,” anatero a Banda. Mayi Dorothy Jailosi a mmudzi mwa Chikula mfumu Kalumba anayamikira boma powalimbikitsa iwo ndikuwapatsa ana awo onse awiri katemera wachikuku pamene anawa anadwala mwa kayakaya. A Jailosi adalimbikitsa amayi onse kuti asamanyalanyaze koma kupita ndi ana awo kokalandira katemera ngati njira imodzi yowatetedza anawo ku miliri yoopsa yomwe ingathe kutenga miyoyo yawo.

ZA UMOYO

Zipatala zatsopano zithandiza ku Neno

WOLEMBA
ROSELYN PHIRI

ANTHU am’boma la Neno ndi osangalala ndi chitukuko cha zipatala zinayi zing’ono zing’ono zomwe zikumangidwa m’bomali ndi Unduna wa Zaumoyo ndi thandizo la ndalama zosachepera 1.1 biliyoni kwacha zochokera ku bungwe la Global Fund. Zipatalazi zikumangidwa limodzi ndi nyumba ziwiri zokhalamo anthu ogwira ntchito pachipatala chilichonse, komanso zikhala ndi magetsi a mphamvu ya dzuwa. Ntchito yomanga zipatalazi inayamba mwezi wa Sepitembala mchaka cha 2022 ndipo ikuyembekezeka kutha mmiyezi iwiri ikubwerayi

chaka chino cha 2024. Akuluakulu ochokera ku Unduna wa Zaumoyo komanso ku bungwe la Global Fund anakayendera ntchito yomanga ziwiri mwa zipatalazi, kwa a Gonthe ndi Feremu kwa Mfumu Mlauli. Atamaliza kuyendera ntchito yomanga zipatalazi ikuyenda bwino ndipo chiyembekezo chilipo kuti ziyamba kugwira ntchito posachedwapa. “Makontilakita athu akuonetsa kuti amaliza ntchito yomanga zipatalazi ikuyenda bwino ndipo chiyembekezo chilipo kuti ziyamba kugwira ntchito posachedwapa. “Makontilakita athu akuonetsa kuti amaliza ntchito yomanga zipatalazi ikuyenda bwino ndipo chiyembekezo chilipo kuti ziyamba kugwira ntchito posachedwapa.



Nyumba zatsopano za ogwira ntchito pa chipatala

kulandira thandizo lamankhwalu pafupi,” anatero Joshua. Iwo adalimbikitsanso anthu a m’bomali kuti adzakhale tatsogolo kusamalira zipatalazo dzikazayamba kugwira ntchito. Mfumu Gonthe, yomwe yachita mwayi olandira chipatala ku dera kwake anati anthu kuderali akukumana ndi mavuto chifukwa amayenda mitunda itali itali kupita kukapeza

thandizo kuchipatala chifukwa chakuti mudera lake mulibe chipatala cha boma pafupi ndipo anati ntchito yomanga chipatala ichepetsa mavutowa. “Ndife osangalala ndikubwera kwa chipatala chimenechi chifukwa tsopano thandizo tizilipeza mdera lathu lomwe lino komanso munthawi yake. Pano timayenda mtunda wautali kupita kuchipatala kwa Magareta ndipo timaoloka mitsinje yambiri kuti tikafike kumeneko,” Mfumuyi inatero. Mmodzi mwa amayi ochokera mdera la Feremu, a Afinesi Feremu anati ndiokondwa kwambiri ndi chitukuko chimenechi chifukwa tsopano azikwanitsa kulandira thandizo lachipatala pafupi.

BOMA LATHU

Nyuzipepala

Mlangizi

William malimero

Mkonzi

Daniel Kasondo

Dizayinala wamkulu

Eugene Makwakwa

Dizayinala wachiwiri

Annie Kakolo

Nyuzipepalayi imafalitsidwa ndi Unduna wa Zofalitsa nkhani

P/Bag 310, Capital City, LL3

www.ict.gov.mw

Boma Lathu nyuzipepala inakhazikitsidwa ndicholinga chophunzitsa ndi kudziwitsa mtundu wa Amalawi popititsa patsogolo ntchito zachitukuko.

SEED CO

LIPIRANI MBEU ZA SEED CO PANG’ONO PANG’ONO POGWIRITSA NTCHITO BANKI

ZOYENERA KUCHITA KUTI MUGULE

- Sankhani mtundu wa mbeu ndi kuchuluka kwake
- Yambani kulipira pang’ono pang’ono ku banki yomwe muli nayo pafupi popanga dipoziti ku ma akaunti omwe apelekedwa m’mumsimu polemba Seed Co Malawi Ltd.
- Tidziwitseni nthawi yomwe mukufuna kudzatenga mbeu yanu ndipo ife tidzakuthandizani.

NB: KUMBUKIRANI KUSUNGA MA DEPOSIT SLIP.

BANKI ZOMWE MUNGAKALIPIRE

Standard Bank

9100001252647

NBS Bank

19302172

FDH Bank

1970000059857

NB National Bank of Malawi plc

1277502

First Capital BANK

0000740139002

THE HOME OF BUMPER HARVESTS

It starts with the right seed | www.seedcoonline.com/mw

SEED CO

LIPIRANI MBEU ZA SEED CO PANG’ONO PANG’ONO POGWIRITSA NTCHITO BANKI

Alimi alimbikitsidwa kusamala fodya

WOLEMBA
LEVISON LESTER

DZIKO la Malawi limadalira ulimi pachuma chake. Imodzi mwa mbewu imene imalimidwa ndikubweretsa ndalama zambiri mdziko muno ndi Fodya. Fodya kuti achite bwino pamsika ndikubweretsa phindu kwa alimi amayenera kuti asamalidwe bwino ndikupereka chikoka kwa ogula.

Mlembi wamkulu mu Unduna wa Zamalimidwe owona za ukadaulo a Medrina Mloza Banda anati malonda a fodya ndiwofunika kwambiri pa chitukuko chachuma cha dziko lino choncho pofunika alimi azigwirana manja potetedza ulimiwu ndi kukhulupirika pa ulimi wa fodya.



Chaka chino kukhala fodya wambiri - Malunga

Polankhula pamsonkhano wa makampani a fodya posachedwapa, mumzinda wa Lilongwe, Mloza Banda anati kasamalidwe kabwino ka fodya ndi kofunika chifukwa zimathandiza kuti tsamba la fodya liziwoneka bwino

pamsika. “Kasamalidwe kabwino ka fodya kamathandiza kukopa ogula ambiri komanso kugula pamtengo wabwino. Ogula amatsata fodya yemwe ali owoneka bwino ndi opereka chikoka pamaso choncho

■ kusamala fodya kungathandize kukweza ulimiwu kupita mtsogolo,” anatero Mloza Banda.

Iwo anati boma likukambirana ndi okhuzidwa pamalonda a fodya za momwe angathanirane ndi mavuto omwe akukhudza ulimiwu chifukwa cha kusintha kwa nyengo.

“Mogwirizana ndi bungwe la Tobacco Commission (TC), boma likukambirananso ndi anthu ndi makampani ogwira nawo ntchito za ulimiwu momwe angachepetsere mavuto omwe ulimiwu ukukumana nawo. Pomwe zokambirana zikupitilira, boma likuyendetsa kale ntchito za ulimi wamthirira zomwe tikukhulupirira kuti zifalikira m’dziko lonse ngati mbali imodzi yoyang’ana madera ena achitukuko

Wojambula: Nkhoswe yathu

ZA ULIMI

WOLEMBA
ALIKO MUNDE

PAMENE alimi ambiri m’Malawi amadalira ulimi wa mvula, Mayi Jane Mtambo a mmudzi mwa Sendelera mdera la Mfumu Mwenewenya m’boma la Chitipa wapeza golide pa ulimi wamthirira.

Mayiwa omwe ndi a zaka makumi asanu ndi chimodzi (51) akuti akunong’oneza bondo chifukwa chotaya nthawi pa ulimi odalira mvula, ndipo ati ulimi wamthirira ndi wopindulitsa kwambiri kuposa wamvula.

“Ulimi wothirira wasintha zinthu. Ndakhala ndikusowa chakudya chaka ndi chaka chifukwa ndinkangodalira ulimi wa mvula,” akutero a Mtambo.

Mayi Mtambo ndi m’modzi mwa alimi 437 omwe akuchita ulimi wamthirira ku sikimu yaku Mafinga imene ili ndi mahekitala 131 ku Chisenga, mdera la Mfumu Mwenewenya m’bomalo.

Sikimu ya Mafinga inakhazikitsidwa ndi ntchito yoona za chitukuko cha ulimi wa mthirira yotchedwa PRIDE ndi ndalama zokwana K1 biliyoni.

Ntchito ya PRIDE inayamba



A Kawale (kumanja) kucheza ndi mmodzi mwa alimi ku Chitipa

kumanga sikimuyi mmwezi wa Meyi mchaka cha 2022 ngati mbali imodzi ya zitukuko zochepetsa mavuto akusowa kwa chakudya m’bomali komanso mdziko muno.

“Kumunda wa chimanga ndikuyembekeza kukolola ma kilogalamu 600 omwe ndiokwana matumba 12, olemera 50 kg liri lonse. Cholinga changa ndichakuti

ndigulitse matumba angapo ndi kusunga ena ngati chakudya chapanyumba.

“Nditakolola chimangachi, ndikukonzekera kubzala mbatata zakachewere ndipo ndikuganiza zogulanso gawo lina la malo la ulimi wothirira kuti ndikhale ndi magawo awiri a mbatatesi,” anatero mai Mtambo.

A Mtambo akupempha

alimi ena kuti ayambe ulimi wamthirira ponena kuti ndi njira yothandiza pa ulimi malinga ndikusintha kwa nyengo.

Mtsogoleri wa Ntchitoyi, a Mathias Kanyika, anatsimikizira boma kuti alimi apitilira kusamalira bwino malowa kuti akhale akupindula anthu kwa nthawi yayitali.

“Mmbuyomu takhala tikulephera kuthirira mbewu

kupatulapo ulimi wa fodya,” iwo anatero.

Mkulu wa bungwe loona za fodya mdziko lino, Joseph Chidanti Malunga anati ngakhale akuganiza kuti fodya achulukira chaka chino, kufunikira kwa mbewuyi pa msika wapadziko lonse kudakali kwakukulu moti pali chiyembekezo choti malondawa chaka chino ayenda bwino.

“Chaka chino tikuyembekeza fodya ochulukira okwana ma kilogaramu 250 miliyoni. Tili ndichikhulupiriro choti malondawa akhoza kuposa achaka chatha,” anatero Malunga.

Iwo analimbikitsanso anthu kuti asamvere zoipa zomwe zimamveka zokhudza ulimi wa fodya ndipo anati anthu anayenera kulowa nawo mu ulimiwu chifukwa ndi opindulitsa komanso umabweretsa chuma chambiri mdziko lino.

zathu chifukwa cha kusowa kwa madzi. Koma titamaliza kumanga sikimuyi, takwanitsa kugwiritsa ntchito mahekitala opitilira makumi awiri a malo othirira. Tikakolola mgawo loyamba, tikuyembekezera kuti mgawo lachiwiri tidzagwiritse ntchito mahekitala onse 131,” anatero a Kanyika.

Nduna ya Zaulimi, a Sam Kawale, anati boma likuzindikira zakufunika kolimbikitsa ulimi wamthirira pothana ndi vuto la kusowa kwa chakudya pachifukwa ichi, kupatulapo boma la Chitipa, boma likuchitanso ulimi wa mthirira ngati umenewu mmadera onse a dziko lino.

Iwo anaonjezerapo kuti pano unduna wawo ukuika chuma cha boma komanso chuma chochokera kwa abwezi achitukuko mndondomeko za ulimi wamthirira pofuna kupeza chakudya chokwanira kumabanja onse mdziko lino.

“Cholinga chathu ndikuthetsa njala powonetsetsa kuti alimi mdziko lonse akukolola kawiri kapena katatu pachaka,” anatero a Kawale.

Ndunayi inatinso unduna wa zamalimidwe uwonetsetsa kuti alimi ang’onoang’ono ndi akulu omwe akupatsidwa thandizo loyenerera kuti athe kupititsa ulimi wawo patsogolo.

Wojambula: Nkhoswe yathu

Kukumba mchenga kukupereka chiopsezo

WOLEMBA
LEONARD MASAULI

PAMENE chitukuko chikupitilira kufalikira mizinda, mmatauni ndikumidzi mdziko lino, ntchito yazomangamanga pakati pa makampani komanso anthu ikupitanso patsogolo. Chitukuko cha zomangamanga chimapereka mpanipani wochulukira kunkhani yofukula ndikugulitsa mchenga womangira pomwe anthu tsopano akulowa penapaliponse ngakhale mmitinje ing’onoing’ono kufunafuna mchengawu.

Kafukufuku wa nthambi wa mgwirizano wa mayiko apadziko lonse wa United Nations wati kupatula madzi, mchenganso ndi gawo limodzi la zinthu zomwe zikugwiritsidwa ntchito mochulukira kwambiri pafupipupi matani 50 biliyoni pachaka.

Kupatula kumangira zinthu zosiyanasiyana, mchenga ndi ofunikanso ku zamoyo zina komanso zomera zina mnyanja komanso mmitinje. Kulekera posapereka malire komanso kulimbikitsa malamulo akafukulidwe ka mchenga

kukuononga zachilengedwe ndipo kutha kubweretsa mavuto akulu kutsogolo, mdziko muno.

Kuno ku Malawi, malonda a mchenga tsopano afika pachimake ndipo tsiku ndi tsiku magalimoto akuluakulu amakhala akututa mchenga kuchoka kumadera osiyanasiyana kukathandizira ntchito yazomangamanga.

Mmodzi mwa omwe amachita malonda ofukula ndikugulitsa mchenga, mmudzi wa Tikoliwe mdera la Mfumu Mlonyeni ku Mchinji, a Francis Njobvu anati kwa zaka zambiri tsopano iwo ndi banja lawo akhala akupeza zofuna zawo kudzera mu kufukula mchenga.

Iwo anati kudzera mu malonda a mchengawa amagula zakudya panyumba komanso zina zonse zofunika pamoyo wao.

“Ndinayamba bizinesi yofukula mchenga kalekale ndipo ndimomwe ndimapezera zofuna zabanja langa. Ndinamanga nyumba komanso kugula katundu wina wamnyumba. Takhala tikumvapo a Nyakwawa athu akutiiza kuti tileke kufukula mchenga koma nanga tidya chani poti tinazolowera,” adatero a Njobvu. Nawo a Justina Banda

ZA CHILENGEDWE



Ntchito zokumba mchenga zikufunika Malamulo

anavomereza kuti bizinesi ya mchenga yawasuntha kuchoka mu umphawi ndipo tsopano ali pabwino ponena kuti chitukuko chanyumba mtauni ya Lilongwe chikuthandizira kutukula bizinesi yawo chifukwa anthu akafuna mchenga amalowera mdera lawo.

“Ndimakwanitsa kulipira ndalama ya kusukulu kwa ana anga chifukwa patsiku ndimatha kugulitsa mchenga wa K50,000,” anatero a Banda. Katswiri pankhani

zachilengedwe a Charles Bakolo anati kukumba mchenga mosasamala kwapangisa kuti mchenga uchepe mmitinje yambiri zomwe zikuchititsa mitsinje kukhala yozama kwambiri.

A Bakolo anati mchaka cha 2023, dziko la Malawi linakumana ndi Ngozi ya madzi osefukira ndipo zina zomwe zinachititsa ndi kufukula mchenga mosasamala mmalo osiyanasiyana.

“Mchenga wamnyanja komanso mmitinje umathandizira kusunga zamoyo zina zing’onozing’ono ndipo kufukula mchengawu mosasata malamulo kukupangitsa nthaka kukokoloka , kufa kwa zamoyo zina komanso kupangitsa kuti madzi asamakhale abwino.

“Boma likuyenera kuchitapo kanthu poonetsetsa kuti anthu akutsatira malamulo pamalonda a mchenga ndipo kuti azipasidwa ziphaso zoyenera pantchitoyi,” adatero a Bakolo.

ZA CHITUKUKO

Olemba nkhani azifalitsanso za ulimi wa mthilira

WOLEMBA
BENI BAMUSI

NTHAMBI ya boma ya Greenbelt Authority yalimbikitsa atolankhani kuti azifalitsa nkhani za ulimi wamthirira ndicholinga choti alimi akhale ndi chidwi ndikuyamba ulimiwu.

Polankhula pamsonkhano wa atolankhani,ku Thyolo mkulu woyang’anira ntchito zosiyanasiyana ku nthambiyi, Rachel Silungwe anati atolankhani ndi ofunikira kwambiri popereka zidziwitso zolondola komanso kudziwitsa anthu zantchito zosiyanasiyana zaboma.

Iwo anati ku Thyolo, Greenbelt Authority ili ndi mgwirizano wa mabungwe a boma komanso omwe si a boma monga Mpatsa Holdings yomwe ili ndi minda ya nthochi ku Khonjeni, yomwe ntchito zake ndizofunika kuti anthu azidziwa. .

“Nkhani za ulimi wamthirira zikufunika kuti anthu azidzitsata kudzera mwa ofalitsa nkhani. Mgwirizano waboma ndi Mpatsa Holdings watipindulira ndipo kunafunika nkhani zake anthu azidzidziwa,” anatero Silungwe .

Bungwe la Greenbelt Authority lidatsindika kuti atolankhani ayenera kupanga utolankhani obweretsa



Ntchito za ulimi wamthilira zizifalitsidwa mokwanira

mayankho komanso kuti apewe kupotoza mfundo ponena kuti nkhani zokhala ndi zolakwika zimaononga mbiri ya dziko komanso kubwezeretsa mmbuyo chitukuko.

M’mawu ake, mkulu ofalitsa nkhani m’boma la Thyolo, Yamikani Yapuwa, anati ndi othokoza chifukwa cha zokambiranazi ndipo anati akuyembekeza kuti atolankhani

a m’boma la Thyolo azilemba nkhani zolondola komanso zogwira mtima.Atolankhani a Zodiak, Malawi News Agency, Mzati ndi ena mwa amene anali nawo pazokambiranazi.

Wojambula: Leonard Masauli

Wojambula: Elia Chibwe

ZINA MWA ZITUKUKO ZOMWE ZIKUCHITIKA MDZIKO LINO

- 1** Nyumba zamakono za asirikali ku zikumangidwa ku MERU Garrison mmboma la Chitipa



- 2** Ma ofesi a khonsolo ya Mmbelwa ku Mzimba ali mkati kumangidwa



- 3** Ntchito yomanga mosungira madzi, a chitukuko cha madzi cha Thazima ku Rumphu ili mkati



- 4** Mseu watsopano wa Chitipa kupita ku Ilomba ukatha, uzathandiza kukweza ntchito zachitukuko ndi zamalonda m'bomali



- 5** Kupindula ndi thandizo la chimanga chaulere chomwe boma likupereka kwa anthu omwe akuvutika ndi njala.



- 6** Nyumba zatsopano za a Polisi ku Ndirande mu mzinda wa Blantyre.



- 7** Mai yemwe anakhudzidwa ndi Namondwe wa Freddy ku Phalombe kusangalala ndi thandizo la ndalama.



- 8** Polimbikitsa ulimi mdziko muno, Boma likupitiliza ndondomeko yogulitsa zipangizo za ulimi zotsika mtengo.

Achinyamata 700 aphunzira ntchito zamanja

WOLEMBA
KONDWANI MAGOMBO

UN G A M V E BWANJI utakhala wachinyamata, o s a p h u n z i r a komanso opanda luso lina liri lonse la ntchito ya manja. Mwadzidzidzi nkupeza mwayi ophunzira ntchito, kumaliza maphunzirowo, ndikupatsidwa zida zoyambira ntchitoyo mwaulere!

Uwu ndi mwayi omwe bungwe losunga ndikubwereketsa ndalama la COMSIP lapereka kwa achinyamata oposa 700 omwe aphunzire luso losiyanasiyana mmaboma khumi ndi anayi (14) mMalawi muno pansi pa ndondomeko yotukula luso la achinyamata ku bungweli.

Mwa achinyamatawa pali atsikana awiri, Naomi Zawanda, wa m'mudzi mwa Nsulira, Mfumu yayikulu Chilowamatambe, m'boma la Kasungu, ndi Efre Fredson wa m'mudzi mwa Tsavu, Mfumu yayikulu Kalumo ku Ntchisi, omwe adzithemba posankha maitanidwe omwe anthu ambiri amawaona ngati ndi ntchito ya amuna okha monga ukalipentala ndi kumanga nyumba.

“Ndili wokondwa kukhala kalipentala wamkazi woyamba m'mudzi mwathu. Ndinkafuna ntchito yovuta ndipo ndi imeneyi,” anatero Zawanda, yemwe sukulu yake analekeza fomu 2 chifukwa cha mavuto azachuma.

“Ndikuthokoza kwambiri COMSIP chifukwa cha mwayi wamaphunzirowa, ndipo ndikulimbikitsa atsikana achichepere kuti asamaziyang'anire pansi. Ntchito ili yonse akhoza kugwira ndikupikisananso ndi anyamata bwino lomwe,” anatero Zawanda.

Ku Ntchisi, Efre Fredson wazaka 29, nayenso anatenga ntchito yomwe anthu amati ndiya amuna, yazomangamanga.

Fredson, amene mwamuna wake nayenso amachita ntchito yofanana ndi imeneyi, akusonyeza kale kuti ndi womanga nyumba wofunidwa kwambiri m'mudzi mwake ndi m'madera ena.

“Nditamaliza maphunziro omwe tidachita kwa miyezi itatu, sindinadikire kuti ndikhale ndi zida zoyambira ntchito. Ndinapeza ntchito ndipo



COMSIP ikuphunzitsa achinyamata ntchito zamanja ngati izi

ndimagwiritsa ntchito zida zobwereka mpaka ndinamanga nyumba zitatu, mipanda iwiri ya njerwa, ndi nyumba ya abusa ku Tsavu CCAP,” anafotokoza motero mayi wa ana awiriyu.

Ulendo wa Fredson sukusiyana kwambiri ndi ulendo wa moyo wa Dalileni Paima wa mmudzi wa Kawaka kwa Kalumo mboma lomwelo la Ntchisi. iyenso anaphunzira ntchitoyi miyezi inayi ndipo, monga mnzake, Fredson, anamaliza maphunziro ake azomangamanga ndikulandira zida zoyambira ntchito yake.

Paima nayenso waonetsa ukadaulo ngati womanga nyumba pamene wayimitsa nyumba ziwiri pa Mponela ndipo padakali pano ndi m'modzi mwa omanga nyumba yopemphereramo ya Chindewe St. Peters Anglican m'mudzi mwa Chikhwakhwa.

“Ine ndi mnzanga, Efre, taphunzitsidwa bwino ndipo ntchito zamanja athu zikutsimikizira zimenezi. Tikuthokoza kwambiri maphunzirowa chifukwa atipatsa zinthu zofunika pamoyo,” anatero Paima, pomwe gulu la atolankhani linamuyendera pamalo omanga tchalitchicho.



Kusoka zovala ndi imodzi mwa ntchito achinyamata akuphunzira

ndipo ali m'magulu a COMSIP. Malinga ndi mkulu ofalitsa mauthenga a chitukuko ku bungwe la COMSIP, a Mercy Kayuni, anati bungweli likukhazikitsa ndondomeko yothandiza achinyamata mogwirizana ndi Unduna wa Achinyamata komanso bungwe la TEVETA.

“Cholinga cha ndondomekoyi ndi kuthandiza achinyamata kuyamba mabizinesi, kapena kupeza ntchito zomwe zingawathandize kuchoka mu umphawi wadzaoneni,” anatero Kayuni.

Iwo anati “Maphunzirowa amachitidwa ndi amisiri a TEVETA ochokera m'madera omwe achinyamatawa akuchokera. Lina mwa luso lomwe achinyamatawa akuphunzira ndi monga ntchito yasaluni, kumeta, kukonza njinga zamoto, kuika magetsi, kusoka, kumanga nyumba, kukonza mapai, ukalipentala ndi kuwotcherera zitsulo.”

Kayuni anati pofika kumapeto kwa ntchitoyi mchaka cha 2027, COMSIP ikhala itaphunzitsa achinyamata 4,300 pansi pa ndondomekoyi.

Kupatula maphunziro ndi zida zoyambira ntchito zatsopano zomwe achinyamata amalandila, amathandizidwanso kupeza ngongole yosachepera MK300,000 kuti ayambitse bizinesi zawo

Zina zomwe akugwirizana ndi achinyamatawa asadayambe maphunziro ndikuti aliyense aziphunzitsa achinyamata ena khumi (10) ochokera m'madera awo kuti luso liperekedwe ndikupindulila achinyamata ambiri.

Malinga ndi mkulu wa COMSIP, a Tennyson Gondwe, gulu loyamba linali ndi achinyamata 721 ochokera m'maboma 14 adziko lino omwe anaphunzira kuyambira Malichi mpaka Juni mchaka cha 2023. Ndalama zokwana MK192million ndizomwe zinagwiritsidwa ntchito pogula zida zoyambira gawo loyamba, pomwe ndalama zonse kuphatikizapo kulimbikitsa achinyamata m'magawo osiyanasiyana ndi pafupifupi MK250million.

Ntchitoyi ikuyembekezeka kufikira achinyamata ena 1,789 kuyambira Febuluwale chaka chino cha 2024.

Wolemba: Kondwani Magombo



Chimodzi mwazipinda zatsopano za atsikana pa Sekondale ya Namatubi ku Chitipa

WOLEMBA
ALIKO MUNDE

KUPEZA maphunziro a p a m w a m b a m'madera akumidzi sikukhala kophweka, makamaka kwa mwana wamkazi.

Ophunzira achitsikana ku Chitipa amakumana ndi mavuto ambiri pamaphunziro awo. Mmodzi mwa atskanawa, Esther Kabaghe wa fomu 2 m'bomali, anatsimikizira zamavuto omwe amakumana nawo akamapita kusukulu, ponena kuti amayenda mtunda wa makilomita

khumi kukafika ku sukulu ya sekondale ya Namatubi.

Msungwanayu yemwe ndi wa zaka khumi ndi zisanu, ndipo amachokera mmudzi mwa Chipanje kwa Mfumu yayikulu Mwabulambya m'bomali, wati pamaphunziro ake wakhala akukumana ndi mayesero akulu ofuna kumulepheretsa sukulu.

Iye anati: “Pamene ndinali Fomu 1, anyamata ankandifunsira, ndikumandinena kuti ndikuvutika kuyenda mtunda wautali koma ine ndinkadziretsa kuti sindingapange zazibwenzi ndikusiya sukulu chifukwa cha mtunda.”

Wophunzira wina Christina Musukwa wa zaka makumi awiri ndi chimodzi, anati anapempha makolo ake kuti apeze nyumba yogonamo kufupi ndi sukulu atatopa ndi anyamata omwe nthawi zonse amamutsatira kumufuna akamapita kapena kuchokera ku sukulu.

Christina, yemwe amakhala pafupi ndi msika wa Chendo, anati mitunda yomwe atsikana amayenda chifukwa chosowa zipinda zogonamo mmasukulu, zimalepheretsa atsikana ambiri pamaphunziro awo.

Mavuto omwe akusimba Esther,

ZA CHITUKUKO

Maofesi atsopano akongoletsa Mzuzu

WOLEMBA
TAWONGA MOYO

ALENDO obwera ku Mzuzu, posachedwapa adziuwonera patali kukongola kwa mzindawu chifukwa cha maofesi atsopano amene akumangidwa mwa ukadaulo .

Ntchitoyi ndi imodzi mwa zitukuko zapamwamba zimene zikuchitika mchigawo cha kumpoto ndi thandizo lochokera ku boma la Malawi ndi ndalama zokwana K12.1 biliyoni.

Nyumbayi yomwe ikhale likulu la Mzinda wa Mzuzu mudzakhala maofesi onse akhonsoloyi komanso chipinda chochitiramo misonkhano.

Mkulu wa mzinda wa Mzuzu, Gomezgani Nyasulu, anati ntchitoyi ndi chinthu chapamwamba ku khonsolo ya Mzuzu komanso dziko lonse



Ntchito yomanga nyumba yatsopano ya khonsolo ya mzuzu ili mkati

Wolemba: Tawonga Moyo

la Nkhata Bay, anayamikira boma pa ntchitoyi yomwe akuti idawapatsa mwayi ogwira ntchito ndikutukula moyo wa banja lawo.

“Ndimagwira ntchito yowumba njerwa pano ndipo ndimatha kusamalira banja langa komanso kupeza

zofunika pa moyo pogwiritsa ntchito ndalama zomwe ndimalipidwa pantchitoyo.

“Ndikutha kulipirira ana anga sukulu ndipo zonsezi zikutheka chifukwa cha boma limene lidandipatsa mwayi pa ntchitoyi,” anatero a Kwaliya.

Ntchitoyi yathandizanso

mayi Thokozani Nkhoma, omwe amachokera mdera la Hilltop mu mzinda wa Mzuzu, kupeza ntchito yowumba njerwa

“Ndinkachita bizinezi koma sindimapeza phindu lilirilonse. Koma ntchito imeneyi itakhazikitsidwa mumzinda wathu, ndinalembedwa ntchito yowumba njerwa,” anatero a Nkhoma.

Mkulu oyang'anira ntchitoyi yomanga pamalopa Nyengo Mtawali anati nyumbayi ikhala ndi maofesi oposa makumi asanu.

“Nyumbayi ikumangidwa pafupi ndi bwalo la za achinyamata la Mzuzu Youth Centre lomwenso likumangidwa. Ichi ndi chitukuko chofunika kwambiri kumpoto kuno,” anatero a Mtawali.

Ntchitoyi yalembe anthu okwana zana limodzi ndi makumi asanu ndipo inayambika mwezi wa Febuluwale chaka cha 2022 ndipo ikuyembekezeka kumalizika mchaka cha 2025.



Wojambula: Wanangwa Tembo

Imodzi mwa nyumba zomwe ena mwa okhudzidwa ndi Namondwe amakhalamo

WOLEMBA
SOLISTER MOGHA

NDUNA ya Zamalo a Deus Gumba posachedwapa a n a p e r e k a nyumba makumi atatu kwa anthu omwe anakhudzidwa ndi namondwe wa Freddy kwa mfumu yaikulu Mwambo ku Zomba.

Nyumbazi ndi zina mwa nyumba makumi asanu ndi awiri ndi mphambu zisanu zomwe zamangidwa ndi thandizo lochokera ku bungwe la Dozy Mmobousi.

Poyankhula pamwambo

Mudzi wa Poko usangalala ndi madzi abwino



Wojambula: Vincent Khonje

Amayi kutunga madzi pamjigo okonzedwanso mmudzi wa Poko

WOLEMBA
VINCENT KHONJE

POZINDIKIRA kufunika kwa madzi aukhondo pa umoyo wa anthu, mabungwe ambiri akutengapo mbali poonetsa kuti midzi imene akugwiramo ntchito ikupeza thandizo la madzi aukhondo mosavuta.

Izi zatsimikizika pamene bungwe la Anglican Council in Malawi (ACM) lakonza mijigo yoonongeka mmudzi wa Poko m'boma la Mchinji ngati njira imodzi yothandiza boma kupereka madzi abwino kwa anthu.

Anthu a m'mudzi mwa Poko mboma la Mchinji ndi osangalala

chifukwa pano akupeza madzi mosavuta omwe akutuluka mmijigo yomwe inaonongeka zaka zapitazo.

Izi zathetsa vuto lomwe amakumana nalo kwa zaka zitatu lofuna kupeza madzi aukhondo.

Kwa zaka zitatu zapitazi, anthu a m'mudzi wa Poko ndi madera ozungulira amasowa mtengo ogwira ndi kudalira zitsime zosazama, zomwe zimawayika pachiwopsezo cha matenda osiyanasiyana pa umoyo wawo.

Wapampando wa komiti ya mijigo mmudzi mwa Poko, a Fordrick Mwale, anati mijigo yawo yakhala isakugwira ntchito kwa zaka zitatu.

“Tinkagwiritsa ntchito zitsime zosazama, ndipo zidabweretsa mavuto ambiri munga matenda otsekula m'mimba, makamaka kwa ana,” anatero a Mwale.

Mkulu wa ofesi ya bungwe la ACM, Taonga Chirwa anati

pamene amagwira ntchito mderali pofuna kulimbikitsa maphunzira a ana ankombaphala a Early Childhood Development (ECD) anazindikira kuti ana amasowekera madzi aukhondo.

“Tinaganiza zothandiza ndi kuthetsa vuto lalikululi ndipo bungwe lathu linabwera litakonzeka ndi zipangizo zokonzera mijigo imeneyi, kotero, pano mijigo yomwe siyimagwira ntchito kwa zaka zitatu, yayamba kugwira,” anatero a Chirwa.

Mayi wa m'mudzi mwa Poko, a Telia Kachingwe, anali okondwa kuti apulumutsidwa ku matenda omwe amavutitsa kwambiri ku mabanja awo.

“Kupezeka kwa madzi abwino sikungowonjezera thanzi lathu komanso kwatipulumutsa kumatenda.

“Tsopano zinthu zili bwino kwambiri, ana athu sakudwaladwala ngati kale,” adatero Kachingwe.

Nduna ipereka nyumba 30 ku Zomba

Iwo anayamikira atsogoleri akale adziko lino Dr. Bakili Muluzi ndi Dr. Joyce Banda omwe anasankhidwa ngati a kazembe pantchito zothana ndi mavuto obwera ndi namondweyu, pomwe anati nyumba zomwe zamangidwa ku Zomba ndi ku Phalombe ndi umboni wa ntchito yabwino yomwe akugwira.

Phungu wa kunyumba ya Malamulo wa Zomba Chisi, Mark Botomani anati ndiokondwa chifukwa nyumba zomwe

zinaperekedwazi zitukula miyoyo ya anthu omwe katundu wawo anaonongeka ndi namondwe.

Botomani anapempha kuti boma liganizire zomanga nyumba zambiri popeza kuti anthu amene anakhudzidwa ndi namondweyu ndi ochuluka.

Mmodzi mwa amene analandira nyumbazi, Edina Govati anati anali okondwa ndi thandizo lomwe analandira poti kwa nthawi yaitali anali akugona mchisakasa.



Zina mwa nyumba zatsopano zomwe ena mwa okhudzidwa alandira

ZA UMOYO

Chakwera ayamikira Chitipa potulutsa akatswiri ampira wamiyendo

WOLEMBA
TAWONGA MOYO

MA SE W E R O a m p i r a wamiyendo akuyembekezeka kupita mtsogolo mboma la Chitipa malinga ndikumangidwa kwa bwalo latsopano lazamasewero m'bomali. Boma la Chitipa linadzizidwitsa anthu pochita bwino pamasewero ampira wamiyendo mchaka cha 2023, pomwe zaonetsa kuti mbomali muli ukatswiri pamasewero.

Mtsogoleri wadziko lino, A Lazarus Chakwera posachedwapa anayamikira boma la Chitipa chifukwa chotulutsa akatswiri pamasewero, pomwe anapereka chitsanzo cha katswiri wakale

pamasewero ampira wa miyendo Kinnah phiri ngati mmodzi mwa amene athandizira kutukula masewerowa kuchokera m'bomali.

A Chakwera anati kunali kofunika kuti bomali likhale ndi malo abwino azamasewero potengera mmene bomali likuchitira pa masewerowa. Mtsogoleri yu anayankhula izi pamene anakayendera ntchito yokonza bwalo lazamasewero la chitipa ndi msewu wa Ilomba-Chitipa ikuyendera m'bomali.

“Chitukuko chosiyanasiyana chikuchitika kuno ku Chitipa munga kukonzedwa kwa bwalo la mpira wamiyendoli, ndichitsimikizo chakuti kuno ku Chitipa kutukuka ndipo anthu ayembekezere zabwino zambiri kuchokera ku boma.

“Tsiku lina, ndidzabwera



Wojambula: Chisomo Kanje

Ku Chitipa kukhala bwalo lazamasewero lapamwamba

kuno ndikudzaonera nawo masewero ampira wa miyendo watimu yathu ndi timu yadziko lakunja. Ine ndionetsetsa kuti ntchitoyi imalizidwe

kuti anthu akuno ku Chitipa alandire chitukuko chimenechi ndikuyamba kugwiritsa ntchito,” anatero mtsogoleri yu.

A Chakwera anayamikiranso

ZA CHILENGEDWE

Kutchena zinyalala posamala chilengedwe

WOLEMBA
PRISCILLA PHIRI

KWANTHAWI yaitali mizinda ya mdziko lino yakhala ikukumana ndi vuto losowa njira zabwino zotaira zinyalala. Mmadera ambiri zinyalala zimangopezeka paliponse zimene zimathandizira kufala kwa matenda osiyanasiyana.

Pozindikira kuwopsa kwa mchitidwewu, Amalawi ambiri ayamba kutenga mbali pochetsetsa zinyalala zimene zimachulukira chifukwa chosowa malo abwino otayira zinyalalazi mmadera mwawo.

Ena, zinyalala akuzigwiritsa ntchito ngati njerwa, enanso akumazigwiritsa ntchito pophikira koma tsopano matelala ayamba nawo kugwiritsa ntchito zinyalala posoka zovala zimene anthu

ambiri ayamba kuzikonda.

Kulukaya Sidiki, mzimai yemwe amadziwika ndi bizinesi yosoka zovala yotchewa Glo-Ray Designs Studio mu mzinda wa Blantyre, anati matelala amathandizira kuwononga chilengedwe chifukwa chamasanza omwe amatuluka muntchito yawo.

Sidiki anati anakhazikitsa Glo-Ray Designs Studio ngati bizinesi komanso ngati njira yochepetsa kuwonongeka kwa chilengedwe pogwiritsa ntchito masanza omwe ena amangotaya paliponse.

“Ife timagwiritsa ntchito zovala zimene zimaoneka zakutha komanso zotayidwa. Zovalazi timazipanga kuti zikhalenso zapamwamba komanso zamaonekedwe abwino zimene zimatha kuvalidwanso ndi amai, abambo ngakhaleenso ana,” adatero a Sidiki

Telala wina wa mu mzinda



Wojambula: Nkhoswe yathu

Zovala zopangidwa kuchokera ku zinthu zotayidwa kudzala



Wojambula: Nkhoswe yathu

Anthu ayamba kuzikonda zovala zopangidwa kuchokera ku zinthu zotayidwa - Sidiki

zowonongeka komanso kuchokera kuzinyalala zina zosavuta kupeza munga masaka zimene ndinasoka ndikuwoneka mwamakono mwakuti zikhoza kuvalidwa kumalo komanso kuzochitika zosiyanasiyana,”

anatero Thyolera.

Poyamikira luso la Ranks45 designs, oyimba nyimbo zamakono osiyanasiyana ayamba zamakono mwakuti zikhoza kumazivala pojambulitsira kanema wa nyimbo zawo.

Hilco watulutsa nyimbo yatsopano

WOLEMBA
PETRO MKANDAWIRE

NYIMBO zatsopano zikutuluka pafupifupi tsiku lina liri lonse mdziko muno. Oyimba sakutopa kutulutsa nyimbo pofuna kusangalatsa owatsatira awo kuti apitilize kumvera nyimbo zawo. Pambali potulutsa nyimbo zosangalatsa anthu, oyimbawa amapezanso nthawi yoimba nyimbo zotamanda Mulungu ndikulimbikitsa anthu kuti asamataye mtima poti mu zonse Namalenga amakhala ali nawo.

Ndipo oyimba chamba cha Afro pop, yemwe dzina lake ndi Hilco Ulolo amene amadziwika mwachidule kuti Hilco, watulutsa nyimbo yatsopano posachedwapa imene ikutchedwa kuti ‘Mwayenera.’

Poyankhula ndi Boma Lathu, Hilco anati nyimbo ya Mwayenera ndi yotamanda Mulungu ndipo cholinga chake ndi kudziwitsa okonda nyimbo zake kuti munyengo zonse Mulungu ayenera kumatamandika.

“Ndimaona ngati anthu amakhumudwa ndi nyengo zomwe akudutsamo ndikuyamba kutaya mtima koma Mulungu sasintha ndiye ndaganiza zolimbikitsa okhulupirira anzanga kudzera



Ndaganiza zolimbikitsa okhulupirira anzanga - Hilco

mu nyimbo imeneyi kuti muzonse, Mulungu ali nafe ndipo zonse ndi zotheka,” anatero Hilco.

Mwayenera, yomwe yajambulidwa ndi Tricky ndi Sispence, ndi nyimbo yoyamba yauzimu kutulutsidwa ndi Hilco chiyambireni ntchito yake yoyimba. Nyimboyi yatulutsidwa pamodzi ndi kanema wojambulidwa ndi VJ Ken.

Hilco adatulutsanso nyimbo yakuti ‘Sanyada,’ yomwe anaimba ndi JJ Cee komanso nyimbo zina zotchedwa Forever, Exactly, Chi Bea, Mundiphunzitse ndi Samalireni yomwe anayimba ndi Fungie.

Mtolankhani wodziwika bwino wa walesi ya MBC Radio 2, Joy Nathu, anati akuyembekezera kuti nyimbo ya Mwayenera ikhala nyimbo yotchuka ya uzimu potengera kuti Hilco ndi katswiri woyimba bwino yemwe nyimbo zake zakhala zikuseweredwa mmawailesi ambiri.

“Timamudziwa Hilco ngati Katswiri pankhani zoyimba, choncho kutuluka kwa nyimbo yake yatsopano kukupereka chiyembekezo chakuti anthu ayikonda pakuti ndi yabwino mmaimbidwe ake. Iye ndi oyimba otchuka kuyambira pakanthawi ndipo Amalawi ayembekezere nyimbo zambiri zabwino kuchokera kwa iye, “ anatero Nathu.



WOLEMBA
ALIKO MUNDE

Khola la ng’ombe ndilofunika kwa Angoni

CHIKHALIDWE chilichonse chili ndi zizindikiro zake monga kavalidwe, magule ndi zikhulupiliro zina. Pa zikhaliidwe zonsezi, mtundu wa Angoni, umadziwika ndi kuvala zikopa za nyama. Nyama monga Ng’ombe ndi Khola lakendizofunikirakwambiri kuchikhalidwe cha Angoni.

Posachedwapa ku Mzimba, pamene Inkosikazi imakhazikitsidwa kuchikhalidwe komanso miyambo ya Angoni, inatengeredwa ku khola la ng’ombe komwe mwambo onse unachitikira. Pamwambowu akuluakulu ena amathira ukali wa ndulu ya ng’ombe pachipumi cha Inkosikazi watsopanoyu pomupatsa mphamvu.

Katswiri pa za chikhalidwe, Aupson William Thole, anati Ng’ombe ndi momwe mwagona mphamvu za chuma komanso mphamvu za chikhalidwe cha chingoni. Iye anati pamene munthu wapeza ng’ombe, munthuyo amakhala kuti wapeza chuma komanso pamene mudzi uli ndi

khola zimatanthauza kuti mudziwu uli ndi ulamuliro okhazikika. Thole anati ngati Mayi wakwatiwa gwero lake limakhala khola lang’ombe. “Pamene mayi wakwatiwa mmudzi kudzera mu khola zimatanthauza kuti wapatsidwa kale malowolo ndipo kuti mtundu wakuchimuna wamulola ndikumuvomereza iye.

“Mfumu iliyonse ili ndi khola chifukwa ndiko kuli mphamvu ndi chuma. Khola ndilofunika kwambiri pomanga mudzi mwanjira zosiyanasiyana. Ngati mkazi wakwatiwa koma mamuna sanapereke malowolo (lobola) ana ake sadzapeza cholowa chilichonse,” Thole anafotokoza.

Iye anaonjezanso kuti ngati Mfumu sinapereke malowolo ndipo kuti mkazi sadabwere kudzera kukhola ndipo amwalira palibe mwana m’banja limenelo amene akhoza kudzakhalira mfumu.

“Mayi ayenera kubwera kudzera kukhola, limeneli ndilo khomo lolowera. Khola ndilofunika kwambiri pa chikhalidwe cha chingoni,” Kufunika kwa khola pa chikhalidwe cha Angoni



Mfumu kuvekedwa ufumu mkhola la Ng’ombe

ZA MASEWERO

Mpira wamiyendo udziyambira msukulu - Akadaulo

WOLEMBA
PETRO MKANDAWIRE

TIMU yampirira wa miyendo yadziko lino yakhala isakuchita bwino mmipikisano yosiyanasiyana kwa nthawi yayitali. Ndikale kwambiri pamene timuyi inatengapo chikho mmipikisano yotchuka muno mu afrika.

Akadawulo azamasewero apempha Unduna wa Achinyamata ndi za Masewera kuti ugwire ntchito limodzi ndi Unduna wa Zamaphunziro kukhazikitsa zamasewero msukulu zonse ngati njira imodzi yotukulira masewero ampira wamiyendo ndi ena mdziko muno.

Kadawulo wamasewero a mpira wamiyendo, Kim Kamau, anati dziko lino likuphonya kwambiri maziko achitukuko cha mpira posakhazikitsa

masewerowa mundondomeko yamaphunziro. Iwo anati kukhazikitsa ndondomeko yokhazikika yamasewero msukulu zingathandize kupeza achinyamata aluso lapamwamba kuchokera kumadera onse adziko lino kuphatikizapo akumidzi, zomwe anati zingathandizire kutukula masewera ampira wamiyendo mdziko lino.

“Tinganene kuti mpira wamiyendo ku Malawi sukupita patsogolo. Tikaona mmene tachitira mmbuyomu pa masewerowa ndikuzaona zipangizo zamasewero zomwe tili nazo, tingati sitikupita mtsogolo,” anatero Kamau.

Iwo anati masewero ampira amatulutsa phindu lalikulu ndipo ndi njira yabwino yomwe amalonda angapangire phindu potsatsa malonda awo, choncho akufunika azilowererapo kuthandiza kutukula masewerowa.

la Balaka, Vivah Mandala, anapempha boma ndi mabungwe kuti akhazikitse mipikisano yammadera ndi kumidzi potukula zamasewero poti kumidziko ndikomwe kuli luso lomwe limabisika kusiyana ndi aluso omwe ali mmatauni.

“Oyendetsa zamasewerowa azidziwa kuti mpira wamiyendo umayambira mmaderamu komanso kumidzi. Tidziwenso kuti masewerowa

ali ndikuthekera kokweza chuma chadziko choncho ngati titayambira kusula achinyamatawa kuchokera msukulu tizapindula ngati dziko,” anatero Mandala.

Iwo analangiza adindo kuti azionesetsanso kuti mabwalo azamasewero azikhala abwino nthawi zonse pomwe anati ngati atakhala abwino pali kuthekera kopeza ndalama mosavuta.



Achinyamata ngati awa aziphunzira mpira wa miyendo kuchokera ku sukulu

MASEWERO



Mpira
wamiyendo
uziyambira
msukulu -
Akadaulo

◀ TSAMBA 15

VOL. 46 NO. 5

YAULERE

oma Lathu, Malichi, 2024

Nyasa Big Bullets ndi akatakwe



Pasuwa -
Mphunzitsi wa
Nyasa Bullets

WOLEMBA
ARKANGEL TEMBO

// MAWULE popita munditenge! Mawule popita munditenge," anayimba mofuula mkulu wina ku sitandi ya timu ya Nyasa Big Bullets kwinaku atapanilira ng'oma nkumapanga chipidigiliro.

Uku kunali kusangalala pomwe timu yake ya Nyasa Big Bullets inakhala akatswiri a chikho cha Airtel Top 8 itafafantha timu ya asirikali ya Mafco pabwalo la zamasewero la Kamuzu mu mzinda wa Blantyre.

Masewerowa adali omalizira kutseka sizoni ya 2023.

Timu ya Bullets, imene kwa iwo amene amayinyadira amayitchula kuti, "Mawule" inapseda zikho zonse za mdziko muno osasiyako ndi chimodzi chomwe kuti matimu anzawo ena 15 atengeko.

Bullets idayamba ndikumweta chikho cha FDH kenako chikho cha Castel, cha TNM komanso Airtel Top 8.

Mchakachi anthu ambiri sanaganizire kuti Bullets ikhoza kuchita bwino potengera kuti inali itataya akatswiri ake monga Chimwemwe Idana amene anapita kutimu ya Silver Strikers.

Bullets inaluzaso katswiri wawo pomwetsa zigoli ochokera

mdziko la Nigeria, Babatunde Adepoju.

Adepoju anapita ku dziko la South Africa. Ndipo potengera izi anthu ambiri anatemetsa nkhwangwa pamwala kuti Bullets ivutika kwambiri popanda akatakwewa.

Ndipo sizoni itayamba Bullets inapanga jenkha pomwe inatuluka mchikho cha matimu amu Africa, cha CAF itaphopholedwa ndi anyamata a TP Mazembe a mdziko la DRC.

Itawonetsedwa msana

wanjira, anthu ambiri ananong'onezana kuti Bullets siyilimba.

Ndipo matimu a Silver Strikers ndi Mighty Mukuru Wanderers anayamba sizoni mwamphamvu koma komwe inadzambatukira Bullets aliyense sadamvetse.

Bullets inasewera masewero okwanira 49, ndipo idapambanapo 33, kufanana mphamvu ndi matimu 12.

Anyamata wochokera mu mdzinda wa Ndirandewa

analephera masewero 4 ndipo masewero odziwika amene anagonja anali apakati pawo ndi timu ya Dedza pabwalo la Dedza komanso inagonja ndi Chitipa ku Karonga.

Kupatula kuchita bwino, Bullets inatulutsanso anyamata angapo amene anachita bwino mu sizoni imene yapitayi.

Mwachitsanzo, Patrick Mwaungulu anakhala katswiri wa a katswiri onse ododa chikopa mdziko muno.

Bullets inayamba kale

zokonzekera sizoni ikubwerayi kuti itetedze zikho zonse zimene idasenza mumipikisano yapitayi.

Mwachitsanzo, kukonzekera koyamba timuyi yalembe kale ntchito osewera angapo ngati Lloyd Aaron kuchokera ku timu ya Civil Service.

Timuyi yatenganso goloboyi wa timu ya Tigers, Innocent Nyasulu.

Timuyi yawonjezeranso nthawi kwa osewera ena kuti atumikire timuyi ngati Precious Phiri, Anthony Mfune ndi Ephraim Kondowe. Komanso yabweresa osewera wake wakale, Babatunde.

Timuyi yasiyananso ndi osewera angapo amene awalola kuti akhoza kupita kumatimu ena.

Mwa osewera ena amene yasiyana nawo ndi monga, Chinedu Okafor ndi Collins Okumu wochokera ku Kenya ndi Nigeria.

Bullets yatayanso Eric Kaonga, Mc Fallen Mgwira, Rabson Chiyenda, Rahaman John, Raghteous Banda ndi White Kitseni.

Mphunzitsi watimuyi, Callisto Pasuwa anati siwokhutira ndi zonse anapanga mu sizoni ya 2023 chifukwa akufunabe Bullets ifikire pamlingo woposa apa.



Wojambula: Nyasa Big Bullets FC

Osewera mpira atimu ya Nyasa Bullets kunyadira chikho cha TNM